# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA NKHOTAKOTA M'DZINJA LA 2024-2025

## DZINJA LA 2024/2025 MWACHIDULE

Nyengo ya dzinja ya 2024/2025 ikuyembekezereka kukhudzidwa ndi La Nina wochepa mphamvu. La Nina ndi kuzizira kwa madzi mdera la pakati chakum'mawa kwa nyanja yamchere ya Pacific. Izi zikhala chomwechi mpaka kumayambiriro a chaka cha 2025

Boma la Nkhotakota likuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuposerapo.


## October 2024




Mwezi wa October udzakhala opanda mvula ku Nkhotakota. Madera ochepa ndi omwe akuyembekezereka kudzalandira mvula koma yochepera mulingo wa 10mm

Mphepo yamkuntho ikuyembekezeka mmadera ena

## November 2024





Nyengo yopanda mvula izapitilira mmadera ambiri a boma la Nkhotakota. Koma madera ena akuyembekezeka kulandira mvula ya mulingo wa pakati pa 20-50mm.

Mvula ikuyembekezeka kuyamba mu sabata yomaliza ya mwezi wa November mpaka sabata yachiwiri ya mwezi wa December 2024.


Mphepo ya mphamvu ndi yamukuntho ikuyembekezeka mmweziwu.

## December 2024





Dzinja likuyembekezeka kuyamba pakati pa sabata lomaliza la mwezi wa November ndi sabata lachiwiri la mwezi wa December 2024. Madera ena mwa TA Kafuzila, Nkhotakota Game Reserve ndi Nkhotakota Boma akuyembekezeka kulandira mvula ya mulingo woposera 200mm.
Madera ena akuyembekezeka kulandira mvula ya mulingo wapakati pa 100-200mm

## January 2025




Madera ambiri akuyembekezeka kulandira mvula yoposera 200mm. Koma madera ena a TA Kanyenda ndi mbali zina za Nkhotakota Game Reserve akuyembekezeka kulandira mvula yamulingo wochepera 200mm.
Ng'amba ya matsiku osaposera asanu ndi awiri ikhoza kukhalako madera ena. Chiopsyezo chakusefukira kwa madzi chilipo.


## February 2025




Mwezi wa February ukhalabe wa mvula madera ambiri a m'boma la nkhotakota. Madera ambiri akuyembekezeka kulandira mvula yapakati pa komanso woposerapo.


Chiopsezo cha ng'amba ya masiku osaposera asanu ndi awiri chilipo madera ena a bomali.

## March 2025




Mvula ya mulingo wokhazikika komanso oposerapo ikuyembekezeka m'bomali.
Madera ambiri akuyembekezeka kulandira mvula ya mulingo wapakati pa 200-300mm. Koma Nkhotakota Boma ndi madera ena TA Mphonde akuyembekezeka kulandira mvula ya mulingo oposera 300mm.
Chiopsyezo chakusefukira kwa madzi chilipo.


## April 2024




Nyengo ya dzinja mu boma la Nkhotakota ikuyembekezeka kufika kumapeto pakati pa sabata yoyamba ndi yachitatu ya mwezi wa April 2025.
Madera ambiri akuyembekezabe kulandira mvula ya mulingo wapakati pa 40-100mm. Madera ena a pa Nkhotakota Boma akuyembekezeka kulandira mvula yoposa 200mm

*Mvula ikuyembekezeka kuyamba pakati pa sabata yotsiriza ya November mpaka sabata yachiwiri ya December 2024. Nyengo ya dzinja ikuyembekezeka kufika kumapeto pakati pa sabata yoyamba ndi yachitatu ya April 2025. Nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kutalika masiku a pakati pa 120 mpaka 145.Chiopsezo cha ng'amba yopyola masiku asanu ndi awiri ndichochepa mu January ndi February 2025.*

| NKHOTAKOTA | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 0.1 | 4.4 | 5.0 |
| NOV | 15.9 | 62.0 | 62.6 |
| DEC | 181.8 | 244.9 | 230.0 |
| JAN | 232.5 | 349.1 | 286.2 |
| FEB | 190.5 | 295.2 | 273.7 |
| MAR | 271.4 | 401.4 | 376.3 |
| APR | 84.4 | 125.9 | 212.6 |




**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2024**

**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku: